# Maphunziro a m’Baibulo

Bible studies

# Kufa ndi kuuka kwa Ambuye Yesu

1. Yesu m’Getsemane
2. Yesu anaperekedwa namangidwa
3. Yesu ku bwalo la akulu a Ayuda
4. Yesu kwa Pilato
5. Yesu anapacikidwa pamtanda
6. Anamuika Yesa kumanda
7. Yesu anauka kwa akufa
8. Yesu anaonekera kwa Mariya wa Magadala
9. Zocitika pa njira ya ku Emau
10. Yesu anaonekera kwa ophunzira ake
11. Yesu anawaonekera ku nyanja ya Tiberiya

# 1. Yesu m'Getsemane

**Mateyu 26.36-46**

36Pomwepo Yesu anadza ndi iwo ku malo ochedwa Getsemane, nanena kwa ophunzira ace, Bakhalani inu
pompano, ndipite uko ndikapemphere.
37Ndipo anatenga Petro ndi ana awiri a Zebedayo pamodzi naye, nayamba kugwidwa ndi cisoni ndi
kuthedwa nzeru.
38Pamenepo ananena kwa iwo, Moyo wanga uti wozingidwa ndi cisoni ca kufika naco kuimfa; khalani pano
mucezere pamodzi ndi Ine.
39Ndipo anamuka patsogolo pang'ono, nagwa nkhope yace pansi, napemphera, nati, Atate, ngati nkutheka,
cikho ici cindipitirire Ine; koma si monga ndifuna Ine, koma lou.
40Ndipo anadza kwa ophunzira, nawapeza iwo ali m'tulo, nanena kwa Petro, Nkutero kodi? simukhoza
kucezera ndi Ine mphindi imodzi?
41Cezerani ndi kupemphera, kuti mungalowe m'kuyesedwa: mzimutu uti wakufuna, koma thupi liri lolefuka.
42Anamukanso kaciwiri, napemphera, nati, Atate wanga, ngati ici sicingandipitirire, koma ndimwere ici,
kufuna kwanu kucitidwe.
43Ndipo anabweranso, nawapeza iwo ali m'tulo, pakuti zikope zao zinalemera ndi tulo.
44Ndipo anawasiyanso, napemphera kacitatu, nateronso mau omwewo.
45Pomwepo anadza kwa ophunzira, nanena kwa iwo, Gonani nthawi yatsalayi, mupumule; onani, nthawi
yafika, ndipo Mwana wa munthu aperekedwa m'manja ocimwa.
46Ukani, timuke; taonani, iye wakundipereka wayandikira.

**Mafunso**

1. Kodi Yesu ndi ophunzira ake anapita kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Yesu anapempha ciani kwa Atate ake? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Nanga inu mumapempheranso kuti kufuna kwa Mulungu kucitidwe?
4. Fotokozani citanthauzo ca 'kufuna kwanu kucitike'.
5. Kodi ophunzira a Yesu anacita ciani pamene Yesu anali kupemphera? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Yesu ananena ciani atapemphera kacitatu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Pezani mau ndipo lembani yankho

| | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| C | P | N | K | H | O | P | E | I |
| I | E | N | P | E | T | R | O | M |
| S | M | P | H | I | N | D | I | F |
| O | P | H | U | N | Z | I | R | A |
| N | H | K | U | F | U | N | A | T |
| I | E | D | I | Y | E | G | K | A |
| R | R | I | T | U | L | O | S | T |
| T | O | K | O | M | A | N | U | E |
| G | E | T | S | E | M | A | N | E |

⇨ ……………………………………………………………………

| | |
|---|---|
| cisoni | Getsemane |
| pemphero | ophunzira |
| imfa | nkhope |
| mphindi | Atate |
| kufuna | gona |
| koma | tulo |


# 2. Yesu anaperekedwa namangidwa

**Yohane 18.1-12**
1M'mene Yesu adanena izi, anaturuka ndi akuphunzira ace, kunka tsidya lija la mtsinje wa Kedroni, kumene kunali
munda, umene analowamo iye ndi akuphunzira ace.
2Koma Yudasenso amene akampereka iye, anadziwa malowa; cifukwa Yesu akamkako kawiri kawiri ndi akuphunzira
ace.
3Pamenepo Yudase, m'mene adatenga gulu la asilikari ndi anyamata, kwa ansembe akulu ndi Afarisi, anadza komweko
ndi nyali ndi miuni ndi zida.
4Pamenepo Yesu, podziwa zonse zirinkudza pa iye, anaturuka, nati kwa iwo, Mufuna yani?
5Anayankha iye, Yesu Mnazarayo. Yesu ananena nao, Ndine. Koma Yudase yemwe, wompereka iye, anaima nao
pamodzi. 6Ndipo m'mene anati kwa iwo, Ndine, anabwerera m'mbuyo, nagwa pansi.
7Pamenepo anawafunsanso, Mufuna yani? koma iwo anati, Yesu Mnazarayo.
8Yesu anayankha, Ndati, Ndine; cifukwa cace ngati mufuna Ine, lekani awa amuke;
9kuti akwaniridwe mau amene ati, Mwa iwo amene mwandipatsa Ine, sindinataya mmodzi.
10Pamenepo Simoni Petro pokhala nalo lupanga, analisolola nakantha kapolo wa mkulu wa ansembe, namsenga
khutu lace lamanja. Koma dzina lace la kapoloyo ndiye Malko.
11Pamenepo Yesu anati kwa Petro, Longa Iupanga m'cimakecace; cikho cimene Atate wandipatsa Ine sindimwere ici
kodi?
12Ndipo khamulo ndi kapitao wamkuru, ndi anyamata a Ayuda anagwira Yesu nammanga iye.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la wophunzira wa Yesu amene anampereka. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi yani amene anabwera kumgwira Yesu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi ciani cimene cinacitika pamene Yesu ananena: ‘Ndine’? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Ndi cifukwa ciani Yesu anafuna kuti ophunzira ake amuke? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Mulungu amasunga anthu ake. Fotokozerani ndime ya 9.
6. Kodi Petro anacita ciani monga mwa m’ndime ya 10?
7. Kodi mwaphunzira m’ndime izi?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao kuti mupeze yankho




| | |
|---|---|
| akulu | malowa |
| kugwa | lupanga |
| ndine | iwo |
| Atate | pansi |
| mfumu | Yesu |
| mau | gulu |
| wamkulu | Kedroni |

⇨ ........................................................................................................

# 3. Yesu ku bwalo la akulu a Ayuda

**Mateyu 26.57-75**
57Ndipo iwo akugwira Yesu ananka naye kwa Kayafa, mkuru wa ansembe, kumene adasonkhana alembi ndi akuru omwe.
58Koma Petro anamtsata kutari, kufikira ku bwalo la mkuru wa ansembe, nalowamo, nakhala pansi ndi anyamata, kuti aone cimariziro.
59Ndipo ansembe akuru ndi akuru mirandu onse anafunafuna umboni wonama wakutsutsa Yesu, kuti amuphe Iye;
60koma sanaupeza zingakhale mboni zonama zambiri zinadza. Koma pambuyo pace anadza awiri,
61nati, Uyu ananena kuti, Ndikhoza kupasula Kacisi, ndi kummanganso masiku atatu.
62Ndipo mkuru wa ansembe anaimirira, nati kwa Iye, Subvomera kanthu kodi? nciani ici cimene awa akunenera Iwe?
63Koma Yesu anangokhala cete. Ndipo mkuru wa ansembe ananena kwa Iye, Ndikulumbiritsa Iwe pa Mulungu wamoyo, kuti utiuze ife ngati Iwe ndiwe Kristu, Mwana wa Mulungu.
64Yesu anati kwa iye, Mwatero, koma ndinenanso kwa inu, Kuyambira tsopano mudzaona Mwana wa munthu ali kukhala ku dzanja lamanja la mphamvu, ndi kufika pa mitambo ya kumwamba.
65Pomwepo mkuru wa ansembe anang'amba zobvala zace, nati, Acitira Mulungu mwano; tifuniranji mboni zina? onani, tsopano mwamva mwanowo;
66muganiza bwanji? Iwo anayankha nati, Ali woyenera kumupha,
67 Pomwepo iwo anathira malobvu pankhope pace, nambwanyula Iye; ndipo ena anampanda kofu,
68nati, Utilote ife, Kristu Iwe; wakumenya Iwe ndani?
69Ndipo Petro adakhala pabwalo: ndipo mdzakazi anadza kwa iye, nanena, Iwenso unali ndi Yesu wa ku Galileya.
70Koma iye anakana pamaso pa anthu onse, kuti, Cimene unena sindicidziwa.
71Ndipo pamene iye anaturuka kunka kucipata, mkazi wina anamuona, nati kwa iwo a pomwepo, Uyonso anali ndi Yesu Mnazarayo.
72Ndipo anakananso ndi cilumbiro, kuti, Sindidziwa munthuyo.
73Ndipo popita nthawi yaing'ono, iwo akuimapo anadza, nati kwa Petro, Zoonadi, iwenso uli wa iwo; pakuti malankhulidwe ako akuzindikiritsa iwe.
74Pamenepo iye anayamba kutemberera ndi kulumbira, kuti, Sindidziwa munthuyo. Ndipo pompo tambala analira.
75Ndipo Petro anakumbukira mau amene Yesu adati, Asanalire tambala udzandikana katatu. Ndipo anaturukira kunja, nalira ndi kuwawa mtima.

**Mafunso**
1. Kodi ansembe akuru ndi akuru a mirandu onse anacita ciani monga mwa m'ndime ya 59?
2. Kodi Yesu anayankha bwanji? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi cifukwa ciani mkuru wa ansembe anag'amba zobvala zake? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Petro anayankha ciani pamene anthu ananena kuti iye anali ndi Yesu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Ndi cifukwa ciani Petro anayankha motere? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi mumayankha bwanji pamene ena akubvutitsani cifukwa mukhulupirira mwa Yesu?
7. Petro analira cifukwa anamva cisoni ca chimo lake. Kodi mukumva cisoni ca macimo anu?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao kukapeza yankho

| | | | |
|---|---|---|---|
| 11 | 15 | 13 | 1 |

| | | |
|---|---|---|
| 9 | 25 | 5 |

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 14 | 1 | 12 | 1 | 19 | 9 | 4 | 23 | 1 |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 3 | 9 | 6 | 21 | 11 | 23 | 1 |

| | |
|---|---|
| 3 | 1 |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 26 | 15 | 12 | 1 | 11 | 23 | 1 |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| 26 | 1 | 20 | 8 | 21 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **A** 1 | **B** 2 | **C** 3 | **D** 4 | **E** 5 | **F** 6 | **G** 7 | **H** 8 | **I** 9 | **J** 10 | **K** 11 | **L** 12 | **M** 13 |
| **N** 14 | **O** 15 | **P** 16 | **Q** 17 | **R** 18 | **S** 19 | **T** 20 | **U** 21 | **V** 22 | **W** 23 | **X** 24 | **Y** 25 | **Z** 26 |

# 4. Yesu kwa Pilato

**Mateyu 27.11-31**

11. Ndipo Yesu anaimirira pamaso pa kazembe, ndipo kazembeyo anamfunsa Iye kuti. Kodi Iwe ndiwe mfumu ya Ayuda? Ndipo Yesu anati kwa iye, Mwatero.
12. Ndipo pakumnenera Iye ansembe akuru ndi akuru, Iye sanayankha kanthu.
13. Pomwepo Pilato ananena kwa Iye, Sukumva kodi zinthu zambiri zotere akunenera Iwe?
14. Ndipo sanayankha Iye, ngakhale mau amodzi, kotero kuti kazembe anazizwa ndithu.
15. Ndipo pa Paskha kazembe adazolowera kumasulira anthu mmodzi wandende, amene iwo anafuna.
16. Ndipo pa nthawi yomweyo anali ndi wandende wodziwika, dzina lace Baraba.
17. Cifukwa cace pamene anasonkhana, Pilato ananena kwa iwo, Mufuna kuti ndikumasulireni yani? Baraba kodi, kapena Yesu, wochedwa Kristu?
18. Pakuti anadziwa kuti anampereka Iye mwanjiru.
19. Ndipo pamene Pilato analikukhala pa mpando wakuweruza, mkazi wace anatumiza mau kwa iye, kunena Musacite kanthu ndi munthu wolungamayo; pakuti lero m'kulota ine ndasauka kwambiri cifukwa ca Iye.
20. Koma ansembe akuru anapangira anthu kuti apemphe Baraba, koma kuti aononge Yesu.
21. Koma kazembe anati kwa iwo, Mufuna kuti ndikumasulireni uti wa awa awiri? Ndipo iwo anati, Baraba.
22. Pilato ananena kwa iwo, Nanga ndidzacita ndi Yesu. Wochedwa Kristu?
23. Onse anati, Apacikidwe pamtanda. Ndipo iye anati, Cifukwa ninji? Anacita coipa cotani? Koma iwo anapfuulitsa kopambana, Apacikidwe pamtanda.
24. Koma Pilato poona kuti sanafitse, koma kuti linapambana phokoso, anatenga madzi, nasamba manja pamaso pa khamulo, nati, Ine ndiribe kucimwira mwazi wa munthu uyu wolungama, mudzionere nokha.
25. Ndipo anthu onse anabvomereza, ndi kuti, Mwazi wace uli pa ife ndi pa ana athu.
26. Pomwepo iye anamasulira iwo Baraba, koma anakwapula Yesu, nampereka Iye kuti akampacike pamtanda.
27. Pomwepo asilikari a kazembe anamuka naye Yesu ku bwalo la mirandu, nasonkhanitsa kwa Iye khamu lao lonse.
28. Ndipo anabvula malaya ace, nambveka malaya ofiira acifumu.
29. Ndipo analuka korona waminga, nambveka pamutu pace, namgwiritsa bango m'dzanja lamanja lace; ndipo anagwada pansi pamaso pace, namcitira cipongwe, nati, Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda!
30. Namthira malobvu, natenga bango, nampanda Iye pamutu.
31. Ndipo pamene anatha kumcitira Iye cipongwe, anabvula malaya aja, nambveka Iye malaya ace, namtsogoza Iye kukampacika pamtanda.

**Mafunso**

1. Chulani dzina la kazembe. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Chulani dzina la munthu wandende amene anamasulidwa m'malo pa Yesu. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi mkazi wa Pilato ananena ciani kwa iye? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi anthu anayankha ciani pamene Pilato anafunsa, 'Ndidzacita ciani ndi Yesu?' Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Pilato anacita ciani kuonetsa anthu kuti iye aganiza kuti Yesu sanalakwe? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi asilikari anacita ciani ndi Yesu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Ndi cifukwa ciani Yesu sanamenyere ufulu?
8. Ndi cifukwa ciani izi zonse zafunika kucitidwa kwa Yesu?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao kuti mupeze yankho

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | |
| 1 | 14 | 1 | 13 | 3 | 9 | 20 | 9 | 18 | 1 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | |
| 3 | 9 | 16 | 15 | 14 | 7 | 23 | 5 | | 14 | 1 | 20 | 9 |

| | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | |
| 20 | 9 | 11 | 21 | 15 | 14 | 5 | 14 | 9 |

| | | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | |
| 13 | 6 | 21 | 13 | 21 | | 25 | 1 | | 1 | 25 | 21 | 4 | 1 |

| a | b | c | d | e | f | g | h | i | j | k | l | m |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |

| n | o | p | q | r | s | t | u | v | w | x | y | z |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |

# 5. Yesu anapacikidwa pamtanda

**Luka 23.26-43**
26Ndipo popita naye, anagwira munthu, Simoni wa ku Kurene, alikucokera kuminda, namsenza iye mtanda aunyamule
pambuyo pace pa Yesu,
27Ndipo unamtsata unyinji waukuru wa anthu, ndi wa akazi amene anadziguguda pacifuwa, namlirira iye.
28Koma Yesu anawapotolokera nati, Ana akazi inu a Yerusalemu, musandilirire Ine, koma mudzilirire nokha ndi ana anu.
29Cifukwa taonani masiku alinkudza, pamene adzati, Odala ali ouma ndi mimba yosabala, ndi mawere osayamwitsa.
30Pomwepo adzayamba kunena kwa mapiri, Igwani pa ife; ndi kwa zitunda, Bisani ife.
31Pakuti ngati azicitira izi mtengo wauwisi, nanga kudzatani ndi wouma?
32Ndipo analinso awiri ena, ndiwo ocita zoipa; anatengedwa pamodzi ndi iye kuti aphedwe.
33Ndipo pamene anafika ku malo dzina lace Bade, anampacika iye pamtanda pomwepo, ndi ocita zoipa omwe, mmodzi ku
dzanja lamanja ndi wina kulamanzere.
34Ndipo Yesu ananena, Atate, muwakhululukire iwo, pakuti sadziwa cimene acita. Ndipo anagawana zobvala zace, poyesa
maere.
35Ndipo anthu anaima alikupenya, Ndi akurunso anamlalatira iye nanena, Anapulumutsa ena; adzipulumutse yekha ngati
iye ndiye Kristu wa Mulungu, wosankhidwa wace.
36Ndipo asilikarinso anamnyoza, nadza kwa iye, nampatsa vinyo wosasa,
37nanena, Ngati Iwe ndiwe Mfumu ya Ayuda, udzipulumutse wekha.
38Ndipo kunalinso lembo pamwamba pace, ndilo: UYU NDIYE MFUMU YA AYUDA.
39Ndipo mmodzi wa ocita zoipa anapacikidwawo anamcitira iye mwano nanena, Kodi suli Kristu Iwe? udzipulumutse wekha
ndi ife.
40Koma winayo anayankha, namdzudzula iye, nati, Kodi suopa Mulungu, poona uli m'kulangika komweku?
41Ndipo ifetu kuyenera; pakuti tirikulandira zoyenera zimene tinazicita: koma munthu uyu sanacita kanthu kolakwa.
42Ndipo ananena, Yesu, ndikumbukileni m'mene mulowa Ufumu wanu.
43Ndipo Iye ananena naye, Indetu, ndinena ndi iwe, Lero lino udzakhala ndine m'Paradaiso.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la mwamuma amene ananyamula mtanda wa Yesu. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Yesu anapacikidwa kuti? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Yesu anapemphera Atate ake kuti akhululukire macimo a iwo amene anampacika. Kodi Yesu akwaniritsa kukhululukiranso macimo anu?
4. Ndi ciani comwe cinalembedwa pamwamba pace? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Yesu ndiye Mfumu?
6. Mmodzi wa ocita zoipa anaopa Mulungu (ndime ya 40) cifukwa anadziwa kuti anacita zoipa pa maso pa Mulungu. Kodi mumaopanso Mulungu cifukwa ca zoipa zanu?
7. Kodi munthuyo anapempha ciani Yesu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
8. Kodi mumapempha ciani?

**Sewero**

Pezani mau

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| M | T | A | N | D | A | W | I | R | I | S | Z | V |
| U | D | Y | F | C | N | C | N | A | P | I | O | Z |
| L | H | U | U | K | U | O | P | A | U | F | U | O |
| U | J | D | R | R | B | D | M | M | G | G | F | B |
| N | Y | A | R | I | S | S | U | T | J | H | U | V |
| G | E | H | K | S | H | F | I | R | K | J | M | A |
| U | S | S | I | T | M | Y | A | N | A | K | U | L |
| K | U | K | H | U | L | U | L | U | K | I | R | A |

- Yesu
- zobvala
- Kristu
- ana
- kuopa
- awiri
- ufumu
- mtanda
- kukhululukira
- zoipa
- Mulungu
- Mfumu
- Ayuda

## 6. Anamuika Yesa kumanda

**Mateyu 27.45-50**

45Ndipo ora lacisanu ndi cimodzi panali mdima pa dziko lonse, kufikira ora lacisanu ndi cinai.
46Ndipo poyandikira ora lacisanu ndi cinai, Yesu anapfuula ndi mau akuru, kunena, Eli, Eli, lama sabakitani? ndiko kunena kuti, Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji Ine?
47Ndipo ena a iwo akuimirira komweko, pamene anamva, ananena, Uyo aitana Eliya.
48Ndipo pomwepa mmodzi wa iwo anathamanga, natenga cinkhupule, nacidzaza ndi vinyo wosasa, naciika pabango, namwetsa Iye.
49Koma ena anati, Taleka, tione ngati Eliya adzafika kudzampulumutsa.
50Ndipo Yesu, pamene anapfuula ndi mau akuru, anapereka mzimu wace.

**Mateyu 27.57-60**

57Ndipo pamene panali madzulo, anadza munthu wacuma wa ku Arimateya, dzina lace Yosefe, amene analinso wophunzira wa Yesu;
58yemweyo anapita kwa Pilato, napempha mtembo wa Yesu. Pomwepo Pilato analamula kuti uperekedwe.
59Ndipo Yosefe anatenga mtembo, naukulunga m'nsaru yabafuta yoyeretsa,
60 nauika m'manda ace atsopano, osemedwa m'mwala, nakunkhunizira mwala waukuru pakhomo pa manda, nacokapo.

**Mafunso**

1. Kodi Yesu anapfuula ciani pa ora lacisanu ndi cinai? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Yesu anasiyidwa ndi Mulungu kuti anthu ake sadzasiyidwe ndi Mulungu. Kodi ndinu mwana wa Mulungu? Kodi mudziwa bwanji ici?
3. Kodi Yesu anacita ciani monga mwa m’ndime ya 50?
4. Chulani dzina la munthu amene anapita kwa Pilato. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi anamfunsa ciani Pilato? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Yosefe, munthu wacuma wa ku Arimateya, anacita ciani ndi thupi la Yesu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi thupi la Yesu linaikidwa kuti? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao kukapeza yankho monga ilembedwa m'Aroma 6.8

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 11 | 15 | 13 | 1 | | 14 | 7 | 1 | 20 | 9 |

| | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 9 | 6 | 5 | | 20 | 9 | 14 | 1 | 6 | 1 | | 14 | 4 | 9 |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| 11 | 18 | 9 | 19 | 20 | 21 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 20 | 9 | 11 | 8 | 21 | 12 | 21 | 16 | 9 | 18 | 9 | 18 | 1 |

| | | | |
|---|---|---|---|
| 11 | 21 | 20 | 9 |

| | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 20 | 9 | 26 | 1 | 11 | 8 | 1 | 12 | 1 | 14 | 19 | 15 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 13 | 15 | 25 | 15 | | 14 | 4 | 9 | | 9 | 25 | 5 |

| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |
| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |

# 7. Yesu anauka kwa akufa

**Mateyu 28.1-15**

1. Ndipo popita dzuwa la Sabata, mbanda kuca, tsiku lakuyamba la sabata, anadza Mariya wa Magadala, ndi Mariya winayo, kudzaona manda.
2. Ndipo onani, panali cibvomezi cacikuru; pakuti mngelo wa Ambuye anatsika Kumwamba, nafika kukunkhuniza mwalawo, nakhala pamwamba pace.
3. Kuonekera kwace kunali ngati mphezi, ndi cobvala cace coyeretsa ngati matalala
4. Ndipo ndi kuopsa kwace alondawo ananthunthumira, nakhala ngati anthu akufa.
5. Koma mngelo anayankha, nati kwa akaziwo, Musaope inu; pakuti ndidziwa inu mulikufuna Yesu, amene anapacikidwa.
6. Iye mulibe muno iai; pakuti anauka, monga ananena. Idzani muno mudzaone malo m'mene anagonamo Ambuye.
7. Ndipo pitani msanga, muuze ophunzira ace, kuti, Wauka kwa akufa; ndipo onani, akutsogolerani ku Galileya; mudzamuona Iye komweko; onani ndakuuzani inu.
8. Ndipo iwo anacoka msanga kumanda, ndi mantha ndi kukondwera kwakukuru nathamanga kukauza ophunzira ace.
9. Ndipo onani, Yesu anakomana nao, nanena, Tikuoneni. Ndipo iwo anadza, namgwira Iye mapazi ace, namgwadira.
10. Pomwepo Yesu ananena kwa iwo, Musaope; pitani, kauzeni abale anga kuti amuke ku Galileya, ndipo adzandiona Ine kumeneko.
11. Ndipo pamene iwo analikupita, onani, ena a alonda anafika kumzinda, nauza ansembe akuru zonse zimene zinacitidwa.
12. Ndipo pamene anasonkhana pamodzi ndi akuru, anakhala upo, napatsa asilikariwo ndalama zambiri
13. nati, Kazinenani, kuti ophunzira ace anadza usiku, namuba Uja m'mene ife tinali m'tulo.
14. Ndipo ngati ici cidzamveka kwa kazembe, ife tidzamgwetsa mtima, ndipo tidzakukhalitsani opanda nkhawa.

**Mafunso**

1. Kodi ndani anadza kukaona manda? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi ciani cimene cinacitika pamene mngelo anatsika Kumwamba? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi mngelo anacita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi mngelo ananena ciani kwa akazi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi ndani anakomana akazi pa njira? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi ndi bodza lotani lomwe asilikari anauza Ayuda? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao kukapeza yankho

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | M | | | | |
| | | | A | | | | | | |
| | | | | | | | F | | |
| | | | | | | | B | | |
| | | | | K | | | | | |
| | | | | | N | | | | |
| | L | | | | | | | | |
| | | T | | | | | | | |

⇨ Lembani yankho: ……………………………………………..!

- tsiku
- mantha
- mulibe
- alonda
- Ambuye
- nkhawa
- anga
- akufa

# 8. Yesu anaonekera kwa Mariya wa Magadala

**Yohane 20.11-18**
11 Koma Mariya analikuima kumanda kunja, alikulira. Ndipo m'mene alikulira anawerama chisuzumirire kumanda;
12ndipo anaona angelo awiri atavala zoyera, alikukhala mmodzi kumutu, ndi wina kumiyendo, kumene mtembo wa Yesu udagona.
13Ndipo iwowa ananena kwa iye, Mkazi, uliranji? Ananena nao, Chifukwa anachotsa Ambuye wanga, ndipo sindidziwa kumene anamuika Iye.
14M'mene adanena izi, anacheuka m'mbuyo, naona Yesu ali chilili, ndipo sanadziwe kuti ndiye Yesu.
15Yesu ananena naye, Mkazi, uliranji? Ufuna yani? Iyeyu poyesa kuti ndiye wakumunda, ananena ndi Iye, Mbuye ngati mwamnyamula Iye, ndiuzeni kumene mwamuika Iye, ndipo ndidzamchotsa.
16Yesu ananena naye, Mariya. Iyeyu m'mene anacheuka, ananena ndi Iye mu Chihebri, Raboni; chimene chinenedwa, Mphunzitsi.
17Yesu ananena naye, Usandikhudze, pakuti sinditha kukwera kwa Atate; koma pita kwa abale anga, ukati kwa iwo, Ndikwera kunka kwa Atate wanga, ndi Mulungu wanu.
18Mariya wa Magadala anapita, nalalikira kwa ophunzirawo, kuti, Ndaona Ambuye; ndi kuti ananena izi kwa iye.

**Mafunso**
1. Kodi Mariya anacita ciani pamene anaona kuti mwala wocotsedwa ku manda? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Mariya anaona ciani pamene anaona m'manda? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi cifukwa ciani Mariya anamva cisoni kwambiri? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi ndani amene anakhala m'mbuyo Mariya? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Yesu anamfunsa ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Mariya anacita ciani atakomana Yesu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Tingaone m'nthano iyi kuti Mariya anakonda Yesu ndi mtima wake wonse. Kodi tingaone bwanji ici?
8. Kodi 'kukonda Yesu ndi mtima wako wonse' kutanthauzanji?

**Sewero**

Pezani mau ndipo lembani yankho mogwiritsa nchito malembo osaphedwa

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| A | N | A | U | K | A | A |
| Y | N | E | T | A | T | A |
| I | W | I | N | A | A | R |
| R | U | M | A | N | D | A |
| A | B | A | L | E | K | B |
| M | I | Y | E | N | D | O |
| M | B | U | Y | E | A | N |
| D | I | M | K | A | Z | I |

- Mariya
- Raboni
- manda
- Atate
- Mbuye
- anauka
- miyendo
- abale
- mkazi
- wina

⇨ ........................................................................

## 9. Zocitika pa njira ya ku Emau

**Luka 24.13-35**

13 Ndipo taonani, awiri a mwa iwo analikupita tsiku lomwelo kumudzi dzina lace Emau, wosiyana ndi Yerusalemu mastadiya makumi asanu ndi limodzi.
14 Ndipo iwowa anakambirana nkhani za izi zonse zidacitika.
15 Ndipo kunali m'kukambirana kwao ndi kufunsana, Yesu mwini anayandikira, natsagana nao.
16 Koma maso ao anagwidwa kuti asamzindikire iye.
17 Ndipo anati kwa iwo, Mau awa ndi otani mulandizanawo poyendayenda? Ndipo anaima ndi nkhope zao zacisoni.
18 Ndipo mmodzi wa iwo, dzina lace Kleopa, anayankha nati kwa iye, Kodi iwe wekha ndiwe mlendo m'Yerusalemu ndi wosazindikira zidacitikazi masiku omwe ano?
19 Ndipo anati kwa iwo, Zinthu zanji? Ndipo anati kwa iye, lzi za Yesu Mnazarene, ndiye munthu mneneri wamphamvu m'nchito, ndi m'mau, pamaso pa Mulungu ndi anthu onse;
20 ndikuti ansembe akulu ndi akulu athu anampereka iye ku ciweruziro ca imfa, nampacika iye pamtanda.
21 Ndipo tinayembekeza ife kuti iye ndiye wakudzayo kudzaombola Israyeli, Komatunso, pamodzi ndi izi zonse lero ndilo tsiku lacitatu kuyambira zidacitika izi.
22 Komatu akazi enanso a mwa ife anatidabwitsa, ndiwo amene analawirira kumanda;
23 ndipo m'mene sanapeza mtembo wace, anadza, nanena kuti adaona m'masomphenya angelo, amene ananena kuti ali ndi moyo iye.
24 Ndipo ena a iwo anali nafe anacoka kunka kumanda, napeza monga momwe akazi adanena; koma Iyeyo sanamuona.
25 Ndipo iye anati kwa iwo, Opusa inu, ndiozengereza mtima kusakhulupirira zonse adazilankhula aneneri!
26 Kodi sanayenera Kristu kumva zowawa izi, ndi kulowa ulemerero wace?
27 Ndipo anayamba kwa Mose, ndi kwa aneneri onse, nawatanthauzira iwo m'malembo onse zinthu za iye yekha.
28 Ndipo anayandikira ku mudzi umene analikupitako; ndipo anacita ngati anafuna kupitirira.
29 Ndipo anamuumiriza iye, nati, Khalani ndi ife; pakuti kuli madzulo, ndipo dzuwa lapendekatu, Ndipo analowa kukhala nao.
30 Ndipo kunali m'mene iye anaseama nao pacakudya, anatenga mkate, naudalitsa naunyema, napatsa iwo.
31 Ndipo maso ao anatseguka, ndipo anamzindikira iye; ndipo anawakanganukira iye, nawacokera.
32 Ndipo anati wina kwa mnzace, Mtima wathu sunali wotentha m'kati mwathu nanga m'mene analankhula nafe m'njira, m'mene anatitseguliramalembo?
33 Ndipo ananyamuka nthawi yomweyo nabwera ku Yerusalemu, napeza khumi ndi mmodziwo, ndi iwo anali nao atasonkhana pamodzi,
34 nanena, Ambuye anauka ndithu, naonekera kwa Simoni.
35 Ndipo iwo anawafotokozera za m'njira, ndi umo anadziwika nao m'kunyema kwa mkate.

**Mafunso**

1. Kodi amuna awiri amene anali kuyenda anacokera kuti? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi iwo anapita kuti? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi yani amene anawalondola pa njira? Ndi m’mdime iti mwapeza yankho?
4. Kodi iwo analankhulana za ciani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi amuna awiri ananena ciani za Yesu Mnazarene? Ndi m’ndime izi mwapeza yankho?
6. Kodi amunawa anayembeza ciani monga mwa m’ndime ya 21?
7. Ndi cifukwa ciani amunawa ndiwo okhumudwa kwambiri?
8. Ndi ciani cimene cinacitika pamene iwo ndi Mlendo anakhala pansi ndi kudya mkate? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
9. Kodi amunawa anacita ciani atazindikira kuti Mlendo ndiye Yesu?
10. Kodi tingaphunzire ciani m’ndime izi?

## 10. Yesu anaonekera kwa ophunzira ake

**Yohane 20.19-25**

19 Pamenepo, pokhala madzulo, tsiku lomwelo, loyamba la Sabata, makomo ali citsekere, kumene anakhala akuphunzira, cifukwa ca kuopa Ayuda, Yesu anadza naimirira pakati pao, nanena nao, Mtendere ukhale ndi inu.
20 Ndipo pamene adanena ici, anaonetsa iwo manja ace ndi nthiti zace. Pamenepo akuphunzira anakondwera pakuona Ambuye.
21 Cifukwa cace Yesu anatinso kwa iwo, Mtendere ukhale ndi inu; monga Atate wandituma Ine, Inenso nditumа inu.
22 Ndipo pamene anati ici anawapumira, nanena nao, Landirani Mzimu Woyera.
23 Zocimwa za anthu ali onse muwakhululukira, zikhululukidwa kwa iwo; za iwo amene muzigwiritsa, zagwiritsidwa.
24 Koma Tomasi, mmodzi wa khumi ndi awiriwo, wochedwa Didimo, sanakhala nao pamodzi, pamene Yesu anadza.
25 Cifukwa cace akuphunzira ena ananena naye, Tamuona Ambuye. Koma iye anati kwa iwo, Ndikapanda kuona m'manja ace cizindikilo ca misomaliyo, ndi kuika cala canga m'cizindikilo ca misomaliyo, ndi kuika dzanja langa ku nthiti yace; sindidzakhulupira.

**Mafunso**

1. Ndi yani amene anasonkana? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. M'ndime ya 19 tawerenga kuti zitseko zinali zotsekedwa. Kodi mlendo uyu analowa bwanji mkati?
3. Kodi Yesu anawapatsa moni bwanji? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Ndi ciani cimene Yesu anaonetsa ophunzira ake? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi muganiza kuti cifukwa nciani Yesu anadzionetsa m'njira iyo?
6. Wophunzira m'modzi sanaliko. Chulani dzina la wophunzirayo. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Tomasi anafuna kuona ciani asanakhulupirire kuti Yesu anauka? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Yohane 20.26-31**

26 Ndipo pakupita masiku asanu ndi atatu akuphunzira ace analinso m'nyumbamo, ndi Tomasi pamodzi nao: Yesu anadza, makomo ali citsekere, naimirira pakati, nati, Mtendere ukhale ndi inu.
27 Pomwepo ananena kwa Tomasi, Bwera naco cala cako kuno, nuone manja anga; ndipo bwera nalo dzanja lako, nuliike ku nthiti yanga, ndipo usakhale wosakhulupira, koma wokhulupira.
28 Tomasi anayankha nati kwa iye, Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga.
29 Yesu ananena kwa iye, Cifukwa wandiona Ine, wakhulupira; odala iwo akukhulupira, angakhale sanaona.
30 Ndipo zizindikilo zina zambiri Yesu anazicita pamaso pa akuphunzira ace, zimene sizinalembedwa m'buku ili;
31 koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace.

**Mafunso**

8. Mobwereza ophunzira anasonkhana ndipo Yesu analowa m'nyumba. Kodi Iye ananena ciani kwa Tomasi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
9. Zizindikiro zambiri zalembedwa m'Baibulo kutiphunzitsa ciani kodi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
10. Kodi Mulungu atilonjeza ciani ngati tikhulupirira kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
11. Kodi mumadalira pa Yesu yekha ndi cipulumutso cake?

**Sewero**

Pezani mau kukapeza yankho

| | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| E | Y | Y | E | S | U | B | N | D |
| M | N | E | I | Y | A | A | E | K |
| U | T | A | S | R | M | I | Z | U |
| L | O | I | H | U | B | B | T | T |
| U | M | S | T | O | U | U | S | S |
| N | A | A | U | M | Y | L | E | I |
| G | S | W | N | A | E | O | K | R |
| U | I | N | A | J | W | A | O | K |
| M | U | L | U | N | A | G | U | ! |

- Mulungu
- Ambuye
- Yohane
- Baibulo
- manja
- Yesu
- Tomasi
- Kristu
- zitseko

Lembani yankho:

…………………………………………………………

## 11. Yesu anawaonekera ku nyanja ya Tiberiya

**Yohane 21.1-17**

1 Zitapita izi Yesu anadzionetseranso kwa akuphunzira ace ku nyanja ya Tiberiya. Koma anadzionetsera cotere.
2 Anali pamodzi Simoni Petro, ndi Tomasi, wochedwa Didimo, ndi Natanayeli wa ku Kana wa ku Galileya, ndi ana a Zebedayo, ndi awiri ena a akuphunzira ace.
3 Simoni Petro ananena nao, ndinka kukasodza. Ananena naye, Ifenso tipita nawe. Anaturuka, nalowa m'ngalawa; ndipo m'usiku muja sanagwira kanthu.
4 Koma pakuyamba kuca, Yesu anaimirira pam bali pa nyanja, komatu akuphunzirawo sanadziwa kuti ndiye Yesu.
5 Yesu ananena nao, Ananu, muli nako kanthu kakudya kodi? Anamyankha iye, lai.
6 Koma anati kwa iwo, Ponyani khoka ku mbali ya dzanja lamanja ya ngalawa, ndipo mudzapeza, Pamenepo anaponya, ndipo analibenso mphamvu yakulikoka cifukwa ca kucuruka nsomba.
7 Pamenepo wophunzira uja amene Yesu anamkonda ananena kwa Petro, Ndiye Ambuye. Simoni Petro pakumva kuti ndiye Ambuye, anadzibveka maraya a pathupi, pakuti anali wamarisece, nadziponya yekha m'nyanja.
8 Koma akuphunzira ena anadza m'kangalawa, pakuti sanali kutali ndi mtunda, koma monga mikono mazana awiri, nakoka khoka la nsombazo.
9 Ndipo pamene anaturukira pamtunda, anapenya moto wamakara pomwepo, ndi kansomba kosanjikikako, ndi mkate.
10 Yesu ananena nao, Tenganiko nsomba zimene mwazigwira tsopano,
11 Cifukwa cace Simoni Petro anakwera m'ngalawa nakokera khoka kumtunda lodzala ndi nsomba zazikuru, zana limodzi, ndi makumi asanu ndi zitatu; ndipo zingakhale zinacuruka kotere, kokha silinang'ambika.
12 Yesu ananena nao, Idzani mufisule. Koma palibe mmodzi wa akuphunzira anatha kumfunsa iye, Ndinu yani? podziwa kuti ndiye Ambuye.
13 Yesu anadza natenga mkate napatsa Iwo, momwemonso nsomba.
14 Imeneyo ndi nthawi yacitatu yakudzionetsera Yesu kwa akuphunzira ace, m'mene atauka kwa akufa.
15 Ndipo pamene atafisula Yesu ananena kwa Simoni Petro, Simoni mwana wa Yona, kodi undikonda Ine koposa awa? Ananena ndi iye, Inde, Ambuye; mudziwa kuti ndikukondani Inu. Ananena naye, Dyetsa ana a nkhosa anga.
16 Ananena nayenso kaciwiri, Simoni mwana wa Yona, ukonda Ine kodi? Ananena ndi iye, Inde, Ambuye; mudziwa kuti ndikukondani Inu. Ananena naye, Weta nkhosa zanga.
17 Ananena: naye kacitatu, Simoni mwana wa Yona, kodi undikonda Ine? Petro anamva cisoni kuti anati kwa iye kacitatu, Kodi undikonda Ine? ndipo anati kwa iye, Ambuye, mudziwa Inu zonse; muzindikira kuti ndikukondani Inu. Yesu ananena naye, Dyetsa nkhosa zanga.

**Mafunso**

1. Kodi ophunzira amene anali pa nyanja ya Tiberiya anagwira nsomba iliyonse? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi yani amene anaimirira pa mbali pa nyanja? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Yesu anawafunsa ciani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Ophunzira anayankha kuti alibe kanthu. Ndi ciani cimene Yesu anawauza kuti acite? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Ndi ciani cimene cinacitika ataponya kokha ku mbali ya dzanja lamanja ya ngalawa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Yesu anamfunsa ciani Petro katatu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Ngati Yesu afunsa inunso ngati mumkonda ndi mtima wanu wonse, mungamyankha bwanji?
8. Yesu anauza Petro kuti ayenera kusamalira ana a Mulungu mwa kuwapatsa cakudya ca uzimu (ndime za 15, 16 ndi 17). Kodi cakudya ca uzimu ndi cotani?
9. Nanga ife tingapatse bwanji cakudya ca uzimu ku anthu ena?

**Sewero**

Pezani mau ndipo lembani yankho mogwiritsa nchito malembo osaphedwa

| | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| * | O | R | T | E | P | U | N |
| D | I | S | I | M | O | N | I |
| E | T | Y | B | T | S | S | N |
| Y | O | A | E | T | E | O | Y |
| U | M | I | R | S | N | M | A |
| B | A | E | I | I | U | B | N |
| M | S | W | Y | E | * | A | J |
| A | I | N | A | H | O | Y | A |

Yankho:………………………………………………………………………………………………….(Yohane 21.22)

# Yesu anati kwa iye: Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, azakhala ndi moyo

# Yohane 11.25